

MTSOGOLERI


CHICHEWA - "Heart Guide"

MTIMA WA MUNTHU

"Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga mkati mwanu mzimu watsopano." *Ezek. 36: 26-27.*

Pamene muwerenga kabukuka ndi kuphuzira pa zithunzi-thunzi zace mudzatha kuona cithunzi-thunzi ca mtima wanu. Lolani kuunika kwa Mulungu kukusonyezezi m'mene mtima wanu wakhalira. Dziwani machimo anu ndipo musawakane kuti palibe, cifukwa mau a Mulungu atiuza kuti, "Tikati kuti tiribe uchimo tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kucicotsera cosalungama ciri conse." *I Yoh. 1:8, 9.*

Muli kuweruzidwa ndi Satana kapena ndi Mulungu. Ngati chimo lili kulamulira moyo wanu, musakane koma fuulirani kwa Mulungu. Iye adzasandutsa inu kukhala mfulu mwa Yesu Kristu amene anafika mdziko kudzapulumutsa anthu ochimwa kudzaphwanyanya mphamvu ya Satana ndi uchimo pa ife. Iye ndiye ciombolo cathu. Muli pamaso pa Mulungu woyera amene apenya zobisika zonse m'maganizo a mkati ndi zocita za moyo wanu. "Pakuti maso ace ali pa njira ya munthu aliyense. Napenya moponda mwace monse. Palibe mdima kapena mthunzi wa imfa, kuti ocita zopanda pace abisaleko." *Yobu 34:21-22.*



Pa cithunzi Coyamba tiona kuti "Mtima ndiwo wonyenga koposa ndi wosaciritsika, ndani angathe kuudziwa?" *Yer. 17:9* "Coturuka mwa munthu ndico cidetsa munthu. Pakuti mkati mwace mwa mitima ya anthu muturuka maganizo oipa, zaciwerewere, zakuba, zakupha, zacigololo, masiro, zoipa cinyengo, cinyanso, diso loipa mwano, kudzikuzi, kupusa, zoipa izi zonse zituruka mkati nizidetsa munthu." *Marko 7:20-23.*

NTHIWATIWA itanthauza chimo la dama. **TONDE WA MBUZI** amasulira cifuniro ca makhalidwe a cigololo, ciwerewere. **NKHU-MBA** inena za machimo akulodzera ndi osusuka. **KAMBA** Anena za ulesi. Kusiya nchito zosamalizidwa ndi ufiti. **NYALUGWE** ndi cirombo coopsya ndi cankhanza ndipo cikhala m'malo mwa udani, nkwiyo ndi kupsya mtima koipa. **NJOKA** imasulira nsanje. **CHULE** anena za machimo a dyera ndi cikondi ca pa ndarama cimene cili muzu wa zoipa zonse *I Tim. 6:10.* **SATANA** ali tate wa abodza ndi onse onena bodza. **NYENYEZI** ndi cikumbumtima. Ca Mtima wa munthu aliyense. Pano uli mtima woipitsidwa ndi

zoipa. **DISO LA MULUNGU** limene liona zinthu zonse zimene zicitika mu mtima wa munthu. Palibe zobisika pa maso othwanima a Mulungu. **TIMALULIME TATING'ONO TA MOTO** tozungulira mtima titanthauza cikondi ca Mulungu cozungulira mtima woipa. **M'NGELO** asonyeza Mau a Mulungu. **NKHUNDA** ndi ciziindikiro ca Mzimu Woyera.

CITHUNZITHUNZI CACIWIRI cionetsa **MTIMA WOLAPA** umene uyamba kufuna Mulungu. Pano ayamba kumvera uthenga wa Mulungu ndi kutsegula mtima wace ku cikondi ca Mulungu. Mzimu Woyera awalira ndi kuunika kwa Mulungu kulowamo ndi kupitkitsa mdima wonse. M'ngelo wagwirira lipanga, "Mau a Mulungu amene ali a moyo ndi ocitacita ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyoza kufikira kugawira moyo nazindikiritsa zolingilira ndi zitsimikizo za mtima." *Ahebr. 4:12.* "Mubwereze kunditsuka mphulupulu yanga. Ndipo muniyeretse kundicotsera coipa canga *Masal. 51:2-10.*





cilungamo.” *Pet. 2:24*. Cifukwa cace ati “Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse cilakolako ca thupi. *Agal. 5:16, 25*. Pali ambiri amene adziyesa akristu opembedza amadya mgonero wa Ambuye, amayimba bwino nyimbo za Mulungu, koma ndi nchito zoipa apacika Mpulumutsi wao tsiku ndi tsiku. Pano tipeza Yudasani ndi thumba lace la ndarama amene anampereka Ambuye Yesu ndi ndarama zasiliva makumi atatu. Maunyolo, miyuni malupanga ndi mikunthu zinali m’manja mwa asilikari amene anamgwira Yesu Kristu. usiku. Pakutenga zobvala zace anacita maere kapena wachiona ndani? monga amacita wochova njuga. *Masal. 22:18*. Anamvula Ambuye Yesu zobvala zace zonse ndi kudzitenga, koma Yesu mwini anamkana — nanena kuti “Sitifuna kulumulidwa ndi munthu uyu.”


Asilikari anampyoza m’nthiti zace ndi nthungo ndipo muna-turuka mwazi ndi madzi *Yoh. 19:33-37*. “Cotero inunso mudziweringere inu nokha ofafa ku uchimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu.” *Aroma 6:11-12*. “Pakuti munafa ndipo movo wanu wabisika pamodzi ndi Kristu mwa Mulungu *Akor. 3:3*.

CITHUNZITHUNZI CA CISANU cionetsa mtima wokonzeka ndi woyeretsedwa ndi wopulumutsidwa ndi Mulungu mwa cismo cace. Tsopano ndiye kacisi weni weni wa Mulungu ndi mokha-



CINTHUNZITHUNZI CA CITATU cionetsa makhalidwe eni eni a munthu wochimwa amene Walapadi. Iye aona tsopano kukula ndi kuopsya kwa machimo ace ambiri-mbiri amene Yesu anafera pa Mtanda. Iye wadzadzidwa ndi mlapo cifukwa amvadi cisoni ndi kucuruka kwa machimo ace. “Mulungu ali pafupi ndi iwo a mtima wosweka. Apulumutsa iwo a mzimu wolapadi.” *Masal. 34:18*. “Mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kutichotsera uchimo wonse.” *I Yohane 1:7-9*. “Koma ndidzayang’anira munthu uyu amene ali waumphawi, ndi wa mzimu wosweka, nanthunthumira ndi mau anga.” *Yes. 66:2*. “Ngati udzabvomereza mkamwa mwako Yesu, ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa udzapolumuka.” *Aroma 10:9!*

CITHUNZITHUNZI CACINAI cinena za mkristu amene wapeza mtendere weni weni ndi ciombolo kupyolera ku nsembe ya Ambuyathu ndi Mpulumutsi Yesu Kristu, koma kudzitamandira ine konse konse, iai koma mu Mtanda wa Ambuye wathu Yesu Kristu, amene mwa Iye dziko lapansi lapacidwira ine, ndi ine ndapacidwira dziko lapansi.” *Agal. 6:14*. Yesu anafa pa Mtanda motero kuti ifenso, “titafa kumachimo, tikhale ndi moyo kutsata



lamo Atate. Mwana ndi Mzimu Woyera malinga ndi lonjezano la Ambuye Yesu Kristu. “Ngari wina akonda Ine, adzasunga mau anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo.

M’malo mokhala cimpando caciwerezuro ca ochimwa, mtima wasinthika kukhala wokongola, wopatsa zipatso zabwino za Mzimu Woyera monga cikondi, cimwemwe, mtendere, kudzicepetsa, kuzunzidwa, kufatsa, ubwino, chikhulupiriro, wodziletsa pa zoledzere-tsa ndi zina kuti zonse zikhale zimene zingathe kukondweretsa Mulungu ndi anthu. *Agal. 5:22, 23*.

Cina cimene ticiona ndi kuti angelo akuonekanso kaciwiri. Angelowa apatulidwa kuti atumikire iwo amene adzalandira moyo wosatha, ndi kuwacinjiriza akumuopa Iye. Woipayo naye waimilira pafupi ndi mtima kuyembekezera mwai wakulowamonso m’malo ace. Chifukwa cace tiri kucenjezedwa kudikira ndi kupemphepa, “Cifukwa mdaniyo mdierekezi ali mkango wobuma ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire.” *I Pet. 5:8*. “Dziwani kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa Inu.” *I Akor. 3:16, 6:19, 20*.

CITHUNZITHUNZI CA CISANU NDI CIMODZI ndi com-
vetsa cisoni ndi munthu wobwerera mbuyo. Diso limodzi layamba
kutsinzina (kutseka) kuonetsa kuti wayamba kuzizira ndi kugona
tulo, pamene diso lija likuyang'anayang'ana za pa dziko, ca uku
ndi uko, osacita nazo manyazi konse. Kuunika konse kwadzirala,
zizindikiro zonse zakusonyeza kumva zowawa pamodzi ndi Kristu
sizionekanso. Wazungulidwa ndi mayesero amene akuwagonjera
pang'ono ndi pang'ono m'malo mwa kulakika. Ngakhale aoneka
wopembedza ndi amnzace pamodzi, cikondi ca pa Mulungu mu-
libe, ku carici ali kungobisalako ndipo mtima wace wadzadzidwa
ndi zilako-lako za pa dziko. Nyenyezi ya m'mtima yotanthauzira
cikumbumtima yadzirala. Mtanda siutengedwa mokondwa, cifukwa
wasandulika katundu wolemera. "Dikirani ndi kupemphera, kuti
mungalowe m'kuyesedwa, Mzimutu uli wakufuna, koma thupi
liri lolefuka." *Mat. 26:41.*



Wolungama wangayo adzakhala ndi moyo wocokera m'cikhu-
lupiriro Ndipo ngati abwerera, moyo wanga ulibe kukondwera mwa
iye." *Ahebr. 10:39.* "Kumbukirani mkazi wa Loti." *Luka 17:32.*




CITHUNZITHUNZI CA CISANU NDI CIWIRI Cibvumbu-
lutsa makhalidwe a munthu wobwerera m'mbuyo Mtima wa munthu
amene analandira kuwala ndi kulawa mphoto ya kumwamba ya
Mzimu Woyera, koma tsopano walephera. Munthu amene aumitsa
mtima wace pamene Mulungu alikumfuna iye adzaipaipabe, sanga-
the kukonzeka mwa iye yekha kapena ndi kuyesayesabe ai koma
pakulandira Yesu apo ndipo. Kwa woterowa Yesu mwini ati: "Pali
pamene mzimu wonyansa ukaturuka mwa munthu upyola malo
opanda madzi nafunafuna mpumulo; ndipo posaupeza unena,
Ndidzabwera kunyumba kwanga kumene ndinaturukako; ndipo
pofika, uipeza yosesa ndi yokonzeka. Pomwepo upita nutenga mizi-
mu yina isanu ndi iwiri yoipa yoposa ndi uwu mwini; ndipo makha-
lidwe otsiriza a munthu uyu aipa koposa oyambawo." *Luka 11:24-
26.* "Koma cidawayenera iwo ca nthanthi yoona, Garu wabwerera
ku masanzi ace, ndi nkhumba idasambayi yabwerera kukunkhulira

m'thoke. *2 Petr. 2:22.* Kodi cithunzithunzi cifanana ndi makhalidwe
a mtima wako, mbalewe! Pfulira kwa Mulungu ndi mtima wako
wonse usachedwe. "Lero ngati mudzamva mau ace Musaumitse
mitima yanu." *Ahebr 4:7.* "Yemwe aumitsa khosi atadzudzulidwa
kwambiri, (mtima wace) adzasweka modzidzimuka, palibe comciri-
tsa. *Miy. 29:1.*

**CITHUNZITHUNZI CA 8 CIONETSA WOKAKAMIRA
MACHIMO OSAFUNA KULAPA AYANDIKIRA IMFA.** Imfa
yafika panthawi yosayembekezeka. Zoipa zimene anadziyesa zoko-
ndweretsa zija zatha, tsopano akumana ndi zowawa zenizeni ndi
mphoto yace ya uchimo. Zowawa za kughena ziyembekeza anthu
ace. Ngakhale alikufuna kupemphera sangathe kupeza umodzi ndi
Mulungu amene cikondi cace anacikana nthawi zonse. "Mphoto
yace ya ucimo ndi imfa." *Aroma 6:23.* "Kugwa m'manja a Mulungu
wamoyo nkoopsya." *Aheb. 10:31.* "Ndipo m'Hade anakweza maso
ace, pokhala nao mazunzo." *Luka 16:19-31.*





CITHUNZITHUNZI CA CISANU NDI CINAI cionetsa mkristu Wolakika Wogonjet a mayesero onse oopsya. Pamene alikuyesedwa ndi zamitundu-mitundu akhalabe cilimbire ndi kupirira kufikira cimariziro, popeza ali ndi mphamvu yotha kugonjetera mwa Yesu Kristu. Satana ndi atumiki ace onse azungulira mtima wa okhulupirira, kuyesa kusoceretsa mwana wa Mulungu. Munthu wogwirizira tambula wa vinyo m'dzanja lace lina akubvina kuzungulira m'kristu ndi kuyesa kumkopa iye ndi zokondweretsa za padziko lapansi. Koma mayeserowa sangacite kanthu pa Mkristu wodzipatulayo, wopacikidwa pamodzi ndi Kristu ku uchimo ndi ku dziko. **NYENYEZI ZA CIKUMBUMTIMA** zace zowala bwino. **THUMBA LA NDARAMA LOBVUNDUKUKA** lionetsa kuti si mtima wace wokha ai, komanso ndi ndarama zace zomwe atumikira nazo Mulungu. **MKATE NDI NSOMBA** zimasulira kuti iye akhala ndi moyo wangwiro ndi wosalodzera. Iye sadziononga yekha ndi zakumwa zoledzeretsa.

BUKHU LOBVUNDUKUKA limasulira kuti buku imene alikonda koposa ndilo Baibulo ndipo amalowerenga ndi kuphunziramomasi ku onse. "Adzatisiyantsa ndani ndi cikondi ca Kristu? nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usuwa, kapena zoopsya kapena lupanga kodi? Koma m'zonsezi, ife tilakatu mwa Iye amene anatikonda." *Aroma 8:35-37*. "Yense wakukhala mwa Iye sachimwa." *I Yoh. 3:6-10*. "pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi; ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu." "Koma m'zonsezi, ife tilakatu mwa Kristu amene anatikonda." *I Yoh. 5:45, Aroma 8:37*.

CITHUNZITHUNZI CA KHUMI ife tiona kuti munthu amene anakhala ndi kuyenda ndi Mulungu saopa imfa. Pamene ikwanira nthawi yakucoka pansi pano, adzapita wokondwa, monga mtumwi Paulo atero, "Pokhala naco colakalaka ca cucoka kukhala ndi Kristu, ndiko kwabwino koposa-posatu." *Afil 1:23*. "M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso." *Yoh. 14:1-4*. "Zimene diso silinaziona, ndi khutu silinazimva, nisizinalowa mu mtima wa munthu, Zimene ziri zonse Mulungu anakonzeratu iwo akukonda Iye *I Akor. 2:9*. "Odala akufa akumwalira mwa Ambuye, kuyambira tsopano; inde anena Mzimu, kuti akapumule ku zolemetsa zao: pakuti nchito zao zitsatana nao pamodzi." *Chibv. 14:13*. "Cabwino, kapolo iwo wokhulupirika, lowa m'cikondwerero ca mbuye wako." *Mat. 25:21*.

Tipemphere:

Ambuye Mulungu ndidza kwa Inu ndi zocimwa zanga ndi mtima wanga wouma. Sindingathe kuusintha. Tengani mtima wanga monga momwe wakhalira. Mundilengere mwa ine mtima wangwiro Mulungu. Ndipo mudzadzemo ndi Mzimu Woyera ndi cikondi. Amen.



If you have found salvation in Christ, or have been otherwise blessed through our Gospel literature, please let us know. We would like to thank God with you, and remember you further in our prayers. **Our Heart of Man Book can now be downloaded in 480 different languages onto cell phones, tablets, etc from our website www.angp-hb.co.za.**

For **free** Gospel literature, books and tracts in over 540 languages, write to:

E-MAIL: info@angp.co.za

ALL NATIONS GOSPEL PUBLISHERS

P.O. Box 2191, PRETORIA, 0001, R.S.A.

(A Gospel Literature Mission financed by donations)

(Reg. No. 1961/001798/08)